# Chichewa A: literature – Standard level – Paper 1
# Chichewa A : littérature – Niveau moyen – Épreuve 1
# Chichewa A: literatura – Nivel medio – Prueba 1

Friday 8 May 2015 (afternoon)
Vendredi 8 mai 2015 (après-midi)
Viernes 8 de mayo de 2015 (tarde)

1 hour 30 minutes / 1 heure 30 minutes / 1 hora 30 minutos

---

### Instructions to candidates

- Do not open this examination paper until instructed to do so.
- Write a guided literary analysis on one passage only. In your answer you must address both of the guiding questions provided.
- The maximum mark for this examination paper is **[20 marks]**.

### Instructions destinées aux candidats

- N'ouvrez pas cette épreuve avant d'y être autorisé(e).
- Rédigez une analyse littéraire dirigée d'un seul des passages. Les deux questions d'orientation fournies doivent être traitées dans votre réponse.
- Le nombre maximum de points pour cette épreuve d'examen est de **[20 points]**.

### Instrucciones para los alumnos

- No abra esta prueba hasta que se lo autoricen.
- Escriba un análisis literario guiado sobre un solo pasaje. Debe abordar las dos preguntas de orientación en su respuesta.
- La puntuación máxima para esta prueba de examen es **[20 puntos]**.

2215 – 0523

4 pages/páginas

© International Baccalaureate Organization 2015

https://xtremepape.rs/

Lembani ndemanga pa nkhani **imodzi** yokha. Poyankha funsoli mugwiritse ntchito mafunso onse awiri amene aperekedwa.

**1.**

**Apatsa Mosiyana**

Pawene adakumbukira tsiku loyamba pa koleji. Adapatsidwa chipinda m'mene munali mtsikana wa chaka chachiwiri. Asanalowe m'chipindamo, adamulandira ndi Bob Marley ali *"One love, one heart! Let's get together and feel alright!"* akutuluka m'masipika awiri ali di! di! di! Ndipo m'chipindamo mudatuluka fungo la mafuta amtengo wapatali ndi chifundizi chonunkhira ulemerero ndi chiwofowo.

Pawene mtsikana winayo adamulandira bokosi lake. Pawene anali atadziyika kale pamzere wa kapolo. Mtsikanayo adamwetulira nati: "Ine ndine Vayida," ndipo adamulandira bokosilo. Vayida adavala deresi looneka molemerera, mosalala, loterera, koma lilibe manja kapena khosi, msana wonse uli pamtunda kulekeza m'chiuno, pamtima pakuonekeranso. Pawene adasilira kusalala ndi kuyera kwa msana ndi pamtimapo, kufewa kwa manja ake, kunyezimira kwa tsitsi lake limene linali ngati wigi. Milomo inali ngati duwa la rozi, Vayida adamwetulira ndi mano oyera ngati mpunga wa faya.

"Ndakondwa kuti ndiwe mnzanga muno. Bedi lako ndi ili, moyika zovala zako ndi umu," adatsekulamo. Pokhala pabedi la mnzakeyo, Pawene adamva ngati akukhala muufa. "Uli bwanji tsono, mnzanga?"

"Ine ndili bwino kaya inu. Ine ndine Pawene." *"One Love, what about one heart…?"* Bob Marley adafunsa.

"Uli ndi kadzina kokongola zedi – Pawene. Ungathe kutsekula bokosi lakoli kuti ndikuthandize kuyala bedili."

*"Let's get together and feel alright!"*

Pawene poona mabulangete ndi zofunda za Vayida zikununkhira mafuta, n'kuonanso mtsikanayo, adachita manyazi kutsekula. Munali bulangete limodzi limene adamupatsa tate wake.

"Ndiyala ndekha ndikapumula bwino lino."

"Kutereku ndimati udziwe kuti ndakulandira ndi manja awiri, ndipo ndine wokonzeka kukuthandiza…"

"Zikomo kwambiri, koma mutafuna kundithandiza mukhoza kundibwerekako sopo; ndinayiwala kugula pobwera."

Choncho Vayida adatulutsa sopo yosambira ndi yochapira n'kumupatsanso bafa thawulo ndi patapata zovalira posamba.

"Palibe chifukwa chondibwezera zonsezi chifukwa ndangogulanso zatsopano…" *"Let's get together and feel alright."* Nyimbo idatha.

Pawene adasambira sopo yonunkhira mosiririka kwanthawi yoyamba m'moyo mwake wonse koma mumtima munalibe chimwemwe. Pochoka uko adakapeza mafuta odzola pabbedi lake Vayida mulibe. Atamaliza kudzikonzakonza, adatuluka ndipo adakumana ndi mnzakeyo. Adam'gwira dzanja. "Tiye tikadye!"

Vayida anali ngati wongotsika ndege kuchokera ku Bahamas, ngati sadziwa chilankhulo chilichonse cha m'Malawi koma Chingerezi chokha. Mnsana wake unali pamtundabe, atangobisa mawere okha. Ndipo adanunkhira moti mkazi kaya mwamuna akagundizana naye azingoti apatu pali chilandamoyo!

"Tikatha kudya ndikuonetsa malo onse pa Koleji pano, ndipo ngati ufuna kukayendapo kutawuni tipita patakisii," Vayida atadatero. Akudya, Pawene adamva mtsikana wina: "Koma ndiye wenafe tadza ndi usiwa, kwathu, mwa! Ndinsapato zovala mtsikana wa koleji ngati ino izo? Taonani deresilo." Anzake adaseka. Chifundo cha chakudya chidathera pompo Pawene.

https://xtremepape.rs/

Ataona anzakewo, ambiri aiwo oyera kumaso kokha atapaka zofiira m'zala zakuda, atametameta nzidze n'kulembalemba m'maso ngati buluzi wa pathanthwe, nayonso milomo ili psuu, mitu ili umo kukula, akuyenda ngati akuvina jazi, Pawene adatsimikiza zobwerera kwawo. Adalowa mosambira, nakhoma, nagwada pansi napemphera. "Ambuye mudati ndikasowa bwenzi ndidze kwa inu. Ndadza kwa inu ndi mtima wa misozi kuti mundipatse mtendere. Mundipatse mphamvu zogonjetsera mayeserowa kuti ndisakwiyire aliyense. Ndilimbitseni mtima, Ambuye ndili ndekha…"

Podzuka apo mtima wake udapepuka ndipo polowa m'chipinda chawo adaonetsa nkhope ypmwetulira. "Komatu Pawene ndiwe wokongola zedi!" Vayida adatero. "Nkhope yakoyinso yachibwenzi zedi. Undiuze za kwanu inenso ndikuuza za kwathu ndi moyo wa pano. Ndithokoza Ambuye pondipatsa bwenzi lero. Tiye tikayendepo…?"

Kwa nthawi yoyamba chifikire pa Koleji Pawene adaonetsa nkhope yosangalala pamaso pa Vayida… Usiku adatsekula bokosi la n'kutulutsamo bulangete. Koma kudzazizira ndipo Pawene adanjenjemera kwinaku akumva kunyodola kwa anzake chifukwa cha zovala zonga za agogo. Kenako Vayida adafunsa.

"Kodi chofunda n'chomwechi?"

"Inde koma ndikagula china mawa akandipatsa ndalama."

"Mnzanga sindifuna kuoneka ngati mwini zonse, koma ndikadakonda ukadandikhulupirira ineyo ngati mnzako n'kundifunsa pamene ukufuna thandizo." Adadzuka.

Joly Max Ntaba, *Ndiwe Wekha Mlamu* (1987)

(a) Perekani ndemanga yanu pa momwe mlembi watisonyezera za anthu awiri amene akutenga mbali mu nkhaniyi.

(b) Fotokozani momwe mlembi wagwiritsira ntchito mutu wa nkhaniyi (Apatsa Mosiyana) pofuna kutiwuza za mfundo zazikulukulu za nkhaniyi.



https://xtremepape.rs/

**2.**

**Kalata ya ku Ndende**

Kwa nonse abale ndi alongo kumudziko,
dikhulupirira muli bwino,
popeza mavuto a uko sangapose akuno kundende.
Ndinachimwira inu komanso ndatukwanitsa mpingo,
ndanyozetsa anzanga ndalilitsa amayi,
maka posapeza phindu mwa ine.
Mukanalota amayi,
mimba inakuthodwetsani ija,
mphatso yake n'kutuluka mbava.

Ndipepese pogwiritsa ntchito *toilet paper*li
pokulemberani kalata kuno ku jele.
Matenda ndi nthenda sizidumpha,
yense woponda nthaka ya kuno.
Msamalumbire kuti simungabwere kuno,
popeza chikankhira munthu kuno n'cha zii.
Ngakhale ndili mwamuna,
yemwe ndinasiya mkwazi wodwala'ndi ana kumudziko,
ndine mkwazi wa mphongo inzanga kuno.

Chakudya n'chochita kukunkha n'kukhadzulirana kuno.
Tikadya nyama ndiye kuti kuti alendo adzayendera ndende.
Kuti ugone motakasuka kuno,
n'kulinga uli ndi khobidi lomupatsa mnyapala.
Nkhufi, nsabwe, nsikidzi
zimatiyamwa mwachilendo.
Kuti inu mulione thupi langa lija,
mudzalephera kuugwira msozi.
Kuno nkosazolowereka.

Silvester Kalizang'oma, *Unkalindanji Moyo* (2013)

(a) Perekani maganizo anu pa mfundo zazikuluzikulu zimene ndakatuloyi ikutiphunzitsa?

(b) Fotokozani momwe mlembi wagwiritsira ntchito zokometsera za ndakatulo monga mawu okuluwika m'ndakatuloyi.

https://xtremepape.rs/